Examination No: ……………………………………

# THE MATENJE ZONAL MOCK EXAMINATIONS BOARD

## 2022/2023 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

**(Malikisi 100)**

**Lachinayi, 13Th April, 2023.** **Subject Number P199**

**Time Allowed: 2 $\frac{1}{4}$ hrs**

**01:00pm – 03:15pm**

**Dzina la Sukulu:** ……………………………………………………………………………………

**Dzina la Ophunzira:** ……………………………………………………………………………………
**(Yambani la Bambo)**

**Malangizo**

1. Pepalali lili ndi masamba **8, chonde onetsetsani.**
2. Pepalali lili ndi magawo anayi, **A, B, C** ndi **D**.
3. Lembani dzina lanu ndi lasukulu yanu pa tsamba lililonse pa pepalali.
4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu gawo **A** ndipo muyankhe mafunso onse mu gawo **B, C** ndi **D**.
5. Lembani yankho lanu m'gawo **A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso amugawoli.
6. Yankhani mafunso amumagawo **B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.
7. Yankhani mafunso amugawo **D** pozunguliza lembo lokhoza pa funso lililonse.
8. Perekani pepala lamafunso ndi mayankho anu kwa oyang'anira mayeso ngati nthawi yakwana.

| Question Number | Tick question if answered | Do not write in these columns |
|---|---|---|
| 1 | | |
| 2 | | |
| 3 | | |
| 4 – 14 | | |
| 15 – 17 | | |
| 18 – 22 | | |
| 23 – 24 | | |
| 25 – 26 | | |
| 27 – 28 | | |
| 29 – 33 | | |
| 34 – 36 | | |
| 37 – 39 | | |
| 40 – 41 | | |
| | | |

**Onani Paseli**

## GAWO A (Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso limodzi mwa mafunso awiri ali m'musiwa. Sankhani mutu wa **Chimangirizo** chanu kapena **Kalata** yanu ndipo mawu asachepere **100** komanso asabzole **150**. Kulemba mwaluso ndikokakamiza ndipo yemwe adzalemba mosayenera adzachotseledwa malikisi.

1. Lembani chimangirizo pa mutu uwu, "**PHWANDO LOSAYIWALIKA**."

   **Mwa zina tsatani izi polemba;**

   **Ndime yoyamba**

   - Tsiku lomwe phwandolo lidachitika
   - Kumalo komwe mudasangalalira
   - Idali nyengo yake iti?
   - Kuchuluka kwa anthu omwe adabwera

   **Ndime yachiwiri**

   - Chifukwa chokonzera phwandolo
   - Zinthu zitatu zomwe zidachitika kuphwandoko
   - Chomwe chidachititsa kuti likhale tsiku losayiwalika

   **Ndime yachitatu**

   - Perekani malangizo awiri omwe akuyenera kutsatidwa pamalo azisangalalo ngati zomwe mwatchulazo

**KAPENA**

2. Yerekezani kuti pasukulu panu palibe aphunzitsi okwanira. Lembani kalata kwa Mkulu wa Zamaphunziro wa m'boma lanu.

   **Mwa zina tsatani izi polemba;**

   **Ndime yoyamba**

   - Cholinga cholembera kalatayo
   - Zifukwa ziwiri zomwe zachititsa aphunzitsi kuti achepe pasukulu yanu

   **Ndime yachiwiri**

   - Kuchuluka kwa ophunzira pasukulu yanu
   - Kuchuluka kwa aphunzitsi omwe mukufuna
   - Mavuto omwe mwakumana nawo chifukwa cha kuchepa kwa aphunzitsi

   **Ndime yachitatu**

   - Fotokozani ubwino udzakhalepo ngati boma lingawonjezere chiwerengero cha aphunzitsi

**Poyankhirapo**

**GAWO B: KUMVETSA NKHANI (Malikisi 20)**

3. **Werengani nkhani ili m'musiyi mosamala ndipo muyankhe mafunso onse motsatira malamulo a Chiyankhulo. Malikisi adzachotseledwa kwa wosalemba bwino komanso kwa wosatsatira malamulo onse.**

Banjali linali ndi ana atatu ndi mdzukulu mmodzi. Mwana wa chisamba adali Tsala, Chitsitsamsepe adali Bingo ndipo mzime adali Ulemu. Banja la a Dodolido limakhala m'mudzi mwa a Chimsonkhano. Iwo amakhulupirira kuti kuwongola mtengo mpachiyambi kotero kuti ana akule ndi makhalidwe abwino amayenera kuwalangiza akadali aang'ono. Makolo ena amadzafunsira nzeru zolangizira ana awo poti mutu umodzi susenza denga. Makolowo samafuna kuwalelera ana awo pachilolo kuopa kuti angadzapulukire. Ana a Dodolido adaphunzira bwino ndipo adali pantchito za pamwamba. Ana amaanja ena sadali pantchito zotero kamba koti adatulukira pa windo kusukulu.

Mwana wamkazi m'banjali amavala zovala zopatsa ulemu chifukwa zinali zazitali zopitirira mawondo. Iwo samavala mabuluku othina, siketi zandekesha kapenanso kazimoto. Anyamatanso m'banjali amavalanso zopatsa ulemu. Mwachidule anawa samavala zovala zotukwanitsa makolo. Makhalidwe a ana m'banjali sadali ochititsa chidwi pa kavalidwe kokha ayi komanso samasuta chamba, samamwa mankhwala ozunguza bongo kapenanso mowa, samachotsa zikwangwani zapamsewu kapenanso kudula mawaya amagetsi ndi mapaipi amadzi. Akafuna kuchoka amatsanzika akamaliza kugwira ntchito zonse zapakhomo. Tsiku lina mfumu idayitanitsa banjali kukawapempha kuti ayambitse bungwe lomwe lizithandiza kulangiza achinyamata makamaka powapatsa uphungu woyenera cholinga chakuti mudziwu udzakhale ndi mzika zamakhalidwe abwino. Mfumuyo idatero posankha a Dodolido ndi akazi awo chifukwa ana awo adalinso amakhalidwe abwino, mfumuyo idati, "inunso makolo muli ndi makhalidwe abwino poti mbuzi ndi mkota."

Banja la a Dodolido lidayamba ntchito ija ndipo samapereka uphungu wa makhalidwe ndi mavalidwe okha yi koma chifukwanso derali kunagwa matenda otsegula m'mimba adawonjezeranso mutu wina wa ukhondo. Ziwiri zinayamba kuyendera limodzi m'malangizo omwe banjali limapereka kwa achinyamata. Adawalangiza kuti wachinyamata wamakhalidwe abwino, mavalidwe oyenera ndi waulemu oyenera kukhalanso waukhondo. Pakhomo pa zisesedwa, pakhale bafa, chimbudzi, khitchini, thandala ndi dzenje lazinyalala. Kupewa matendawa tonse tiyenera kudya chakudya chophikidwa bwino, chotentha, tiyenera kusamba m'manja ndi sopo, tisanadye chakudya komanso tikachoka kuchimbudzi. Adawalimbikitsanso achinyamatawa sukulu kotero mudziwu udali ndi anthu ambiri ophunzira bwino, ogwira ntchito zaboma. Udali mudzi wosamalika ndiwochititsa chidwi chifukwa matenda otsegula m'mimba zilumika asanagwireko anthu. Udali mudzi waulemu kamba ka malangizo a Dodolido ndi akazi awo.

**Mafunso**

A. Kodi banja la a Dodolido limakhala m'mudzi wayani?

________________________________________________ (Malikisi 1)

B. Banjali linali ndi ana atatu. Kodi mwana womaliza kubadwa m'banjali adali yani?

________________________________________________ (Malikisi 1)

C. Kodi banjali lidatchuka chifukwa ninji?

________________________________________________

________________________________________________ (Malikisi 2)

D. Mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani ana a m'banjali adali pantchito zapamwamba?

________________________________________________ (Malikisi 1)

E. Tchulani zovala **ziwiri** zomwe Ulemu samavala.

i) ________________________________________________

ii) ________________________________________________ (Malikisi 2)

F. Pezani zinthu **ziwiri** zomwe ana a amuna m'banjali samachita.

i) ________________________________________________

ii) ________________________________________________ (Malikisi 2)

G. Mukuganiza kuti n'chifukwa chiyani anawa amatsanzika akafuna kuchoka pakhomo.

________________________________________________ (Malikisi 1)

H. Kodi bwanji mfumu idayitanitsa banja la a Dodolido?

________________________________________________ (Malikisi 1)

I. Perekani matanthauzo amawu awa;

i) Lelera pachilolo

_______________________________________________ (Malikisi 1)

ii) Mbuzi ndi mkota

_______________________________________________ (Malikisi 1)

iii) Tulukira pawindo

_______________________________________________ (Malikisi 1)

iv) Chitsitsamsepe

_______________________________________________ (Malikisi 1)

J. Tchulani zinthu **ziwiri** zokha zomwe achinyamata ayamba kuzitsatira banja la a Dodolido litayitanidwa ndi mfumu ya m'mudzi.

i) _______________________________________________

ii) _______________________________________________ (Malikisi 2)

K. Kodi wachinyamata wamakhalidwe abwino akuyenera kumatsatira zinthu **ziwiri** ziti malingana ndi nkhaniyi?

i) _______________________________________________

ii) _______________________________________________ (Malikisi 2)

L. Perekani mutu wankhaniyi.

_______________________________________________ (Malikisi 1)

**GAWO C: (Malikisi 10)**

4. **Werengani kankhanika ndi kuyankha mafunso ali m'musiwa;**

"Popeza mwanena kuti wathu ndi gocho ndiye ife timutenga tikamabwerera kwathu koma mumulole kuti atenge chipindatchika chake."

**Mafunso**

a) Kodi ndimalonje anji amenewa?

_______________________________________________ (Malikisi 1)

b) Angalankhule malonjewa ndani?

_______________________________________________ (Malikisi 1)

c) Kodi malonjewa akuchitikira kuti?

_______________________________________________ (Malikisi 1)

d) Perekani tanthauzo la mawu oti, "**chipindatchika**"

_______________________________________________ (Malikisi 1)

e) Lembani kuyipa kumodzi kwa mchitidwe wa ziphuphu.

_______________________________________________ (Malikisi 1)

**KUPANGA ZIGANIZO**

5. **Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu ali m'musiwa kusonyeza kuti mukudziwa matanthauzo ake.**
   a) Mong'ung'udza
   ______________________________ (Malikisi 1)
   b) Msampha
   ______________________________ (Malikisi 1)
   c) Pokhapokha
   ______________________________ (Malikisi 1)
   d) Zitatu
   ______________________________ (Malikisi 1)
   e) Mbwee
   ______________________________ (Malikisi 1)

**GAWO D: (Malikisi 40)**

**Zungulizani lembo lokhoza (A, B, C kapena D) m'mafunso otsatirawa.**

**Mafunso 6 mpaka 11**; sankhani mitundu ya mawu omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

6. **Moyo** umenewu siwabwino.
   A. Dzina  C. Mvekero
   B. Mneni  D. Muonjezi

7. **Tanu** timakonda kusewera.
   A. Mfotokozi  C. Mlowam'malo
   B. Mperekezi  D. Dzina

8. Grace **ndi** wokongola ngati duwa.
   A. Mperekezi  C. Muonjezi
   B. Mneni  D. Mlumikizi

9. Amene **ali** ndi ziwiri andigayire.
   A. Mlumikizi  C. Mneni
   B. Mperekezi  D. Mfotokozi

10. Wadya nthongo zitatu **basi**.
   A. Mfotokozi  C. Mlowam'malo
   B. Muonjezi  D. Mneni

11. Chibwana **chake** chamulepheretsa mayeso.
   A. Mlowam'malo  C. Mperekezi
   B. Dzina  D. Mfotokozi

**Mafunso 12 mpaka 14;** sankhani mitundu ya mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo.

12. Pali **chidani** chachikulu pakati pa Mishel ndi Tanangachi.
   A. Launyinji
   B. Lachinthu chokhudzika
   C. Lamwinimwini
   D. Lachinthu chosakhudzika

13. Abambo asankha **mulu** umodzi wa nsomba.
   A. Lamwinimwini
   B. Lachinthu chokhudzika
   C. Launyinji
   D. La chinthu chosakhudzika

14. Adaoloka pa **mtsinje** popita kwawo.
   A. Lamwinimwini
   B. Lopanda mwinimwini
   C. Lachokhudzika
   D. Lachosakhudzika

**Mafunso 15 mpaka 16;** sankhani mitundu ya nthambi zachiganizo zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo.

15. Anthu **omwe mayina awo alim'kaundula** amaloledwa kuvota.
   A. Ya dzina  C. Ya muonjezi
   B. Ya mfotokozi  D. Ya mneni

16. Taphunzira **zoti tili ndi ufulu wachibadwidwe**.
   A. Ya dzina  C. Ya muonjezi
   B. Ya mfotokozi  D. Ya mneni

**Mafunso 17 mpaka 21;** sankhani misintho ya aneni pozunguliza lembo lolondola m'ziganizo zotsatirazi.

17. Namwali uja **wamenywa**.
    A. Wochitidwa C. Wochitirana
    B. Wonyazitsa D. Wochitira

18. Nkhuku **yamangidwa** ndi chingwe.
    A. Wochitira C. Wochitidwa
    B. Wochitirana D. Wochititsa

19. Chitseko chija **chatsekeka**.
    A. Wochitidwa poyera
    B. Wochitika
    C. Wochitidwa
    D. Wochitidwa m'chibisira

20. **Wayalula** mphasa ija.
    A. Wochitira C. Wochitirana
    B. Wamtsutso D. Woyalula

21. **Walimbikitsa** gululo kutenga ndalama za ngongole.
    A. Wochitsitsa C. Wolimbikitsa
    B. Wochita D. Wochititsa

**Mafunso 22 mpaka 25;** sankhani magulu a mayina m'ziganizo zotsatirazi.

22. Mwana wagwera mu **dzenje** pothamangitsa nkhuku.
    A. U __, Ma __. C. Mu __, Mi __.
    B. I __, Zi __. D. Li __, Ma __.

23. **Ntchentche** ndizomwe zafalitsa matenda otsegula m'mimba.
    A. I __, Zi __. C. Ka __, ti __.
    B. Chi __, Zi __. D. U __, Ma __.

24. Chati deru chidaopsa **mlenje**.
    A. Mu __, Mi __. C. Li __, Ma __.
    B. U __, Ma __. D. Mu __, A __.

25. Adaliyatsa liwiro la **mtondo** wadooka.
    A. Mu __, Mi __. C. Li __, Ma __.
    B. U __, Ma __. D. Mu __, A __.

**Mafunso 26 mpaka 28;** sankhani mitundu ya aonjezi m'ziganizo zotsatirazi.

26. Anangokhala **chete**, osanena kanthu.
    A. Wa malingaliro C. Wa muyeso
    B. Wa mchitidwe D. Wa nthawi

27. Anamudzutsa **m'bandakucha** kuti akasambe.
    A. Wa malingaliro C. Wa muyeso
    B. Wa mchitidwe D. Wa nthawi

28. Ng'ombe zikudya msipu **patsidya**.
    A. Wa dzina C. Wamaonekedwe
    B. Wa malo D. Wa nthawi

**Mafunso 29 mpaka 30;** perekani matanthauzo a mikuluwiko ili m'musiyi.

29. Thawa mtswatswa wako womwe.
    A. Pulumuka
    B. Thawa munthu
    C. Kana chomwe wachita
    D. Nena bodza

30. Lowa mthumba lalikongwe.
    A. Chita mphumi
    B. Peza Mwayi
    C. Peza vuto
    D. Peza likongwe

**Mafunso 31 mpaka 32;** sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera zamkalembedwe.

31.
    A. Anyamatawo adati tidzabwera sabata lamawa.
    B. anyamatawo adati, "tidzabwera sabata lamawa"
    C. Anyamatawo adati "Tidzabwera sabata lamawa."
    D. Anyamatawo adati, tidzabwera, sabata lamawa.

32.
    A. Iwo adachita kaguni (manyazi) atawapeza akuba.
    B. Iwo adachita kaguni / manyazi atawapeza akuba.
    C. iwo adachita kaguni (manyazi) atawapeza akuba
    D. Iwo adachita kaguni, manyazi, atawapeza akuba.

**Mafunso 33 mpaka 34;** sankhani chachikazi cha mayina awa;

33. Nkhunzi
    A. Mtheno
    B. Mkota
    C. Nthoni
    D. Nthondo

34. Muphwa
    A. Mbombe
    B. Mfumakazi
    C. Mkwatibwi
    D. Malume

**Mafunso 35 mpaka 36;** sankhani mikuluwiko yotsutsana m'matanthauzo ndi yomwe ili m'ziganizozi.

35. Apawo ndimizu ya kachere amakumana pansi.
    A. Chili kwa mzako mkumati chigwire nyanga
    B. Pano mpathu adam'gonetsa mkhonde
    C. Zolowere mkudyere mwana
    D. Nkhondo ndi anasi

36. Linda madzi adikhe ndiye udziti ndadala.
    A. Ali mbina kulinga utamtsogoza
    B. Kanthu mkako uvundukula nupenya
    C. Papsa tonola sudziwa mtima wamoto
    D. Kunena kwa ndithe ndithe namnthambwe adadzitengera

**Mafunso 37 mpaka 38;** sankhani nthawi zoyenera m'ziganizo zotsatirazi.

37. Nyengo yamvula **<u>timavutika</u>** popita ndikubwera ku sukulu.
    A. Yakawirikawiri
    B. Yakale
    C. Yamtsogolo
    D. Yatsopano

38. **<u>Ndidzakhala</u>** ndikulemba mayeso pomwe iye adzikalemba.
    A. Yamtsogolo
    B. Yamtsogolo yakawirikawiri
    C. Yatsopano
    D. Yamtsogolo yathayi

**Mafunso 39 mpaka 40;** sankhani mikuluwiko yofanana m'matanthauzo ndi mikuluwiko yotsatirayi.

39. Chikumbutsa nkhwangwa n'chisanu.
    A. Umanena chatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke nyanga
    B. Chibale cha nkhwangwa chokoma pokwera
    C. Ulenje umasimba wako
    D. Chonona chifumira kudzira

40. Alimbina mkulinga utamtsogoza.
    A. Ziliko mkulinga alimbina
    B. Ali dere mkulinga utayenda naye
    C. Pakadafunda padajiwitsa galu
    D. Mutu ukakula sulewa nkhonya

**Mafunso 41. i) mpaka 41. v); lembani ziganizo izi m'ndondomeko yoyenera**

41. i) Omwe ankakhala kutali ndi mudzi omwe iye amakhala.
    ii) Iye adakambirana ndi azakhali ake kufunika kwa maphunziro
    iii) Iwo adamulandira mwansangala.
    iv) Chifuniro adaganiza zogona kwa azakhali ake popeza kudali kutayamba mdima.
    v) Chifuniro adapita kwa agogo ake kukawaona.

**Poyankhirapo**

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

______________________________________________

**MAFUNSO ATHERA PANO**